



KUKWANIRITSA KUPAMBANA KWA AMAYI PA CHISANKHO

**BUKHU LOTHANDIZA AMAYI OFUNA KUKHALA ATSOGOLERI
M'MAKHONSOLO NDI M'NYUMBA YA MALAMULO M'MALAWI**

Gawo Loyamba	:	Chiyambi.....	4
Gawo la Chiwiri	:	Mawu Otsogolera.....	4
		Chisankho cha Pulezidenti	5
		Chisankho cha Aphungu	5
		Chisankho cha Maboma Aang'ono.....	5
Gawo la Chitatu	:	Zina ndi Zina Zokhudza Kayendetsedwe ka	
		Boma.....	6
		Maboma Aang'ono m'Malawi.....	6
		Madera a Maboma Aang'ono m'Malawi	6
		Mphamvu ndi Ntchito za Khonsolo	7
		Boma.....	8
		Ntchito ndi Udindo wa Khansala	10
		Ntchito ndi Udindo wa Phungu	10
		Kukonzekera Chisankho	10
Gawo la Chinayi	:	Gawo la Amayi pa Ndale	11
		N'chifukwa chiyani amayi ayenera kuchita ndale?.....	11
		Mfundo zomwe dziko lino likutsata	12
		Mfundo zomwe dziko lapansi likutsata.....	13
Gawo la Chisanu	:	Mwayi womwe Amayi ali nawo pa ndale ndi	
		Kulimbana ndi Mavuto okhudza Jenda	13
		Kodi pali mwayi wanjii wosankhidwa pa ndale?.....	13
		Mavuto omwe alipo ndi otani?.....	14
		Mfundo zina zofunika.....	15
Gawo la Chisanu ndi Chimodzi	:	Kukopa anthu	16
		Kukopa anthu pa chisankho	16
		Ndani angakope anthu?.....	16
		Kukonzekera ntchito yokopa anthu	16
		Njira zina zokopera anthu.....	16
		Njira zochitira misonkhano yokopa anthu	17
		Malo oletsedwa kukopa anthu	17
		Luso lokopera anthu	17
		Zipsinjo pa kukopa anthu ndi njira zozithetsera.....	18
Gawo la Chisanu ndi Chiwiri	:	Kuthetsa Mikangano	19
		Mikangano ya chisankho	20
		Njira zothetsera mikangano ya chisankho.....	20

GAWO LOYAMBA: CHIYAMBI

Kuchepa kwa chiwerengero cha amayi otenga mbali ndi kuimira anthu m'boma komwe kulipo padakali pano kuno ku Malawi nkosafunika ndipo koyenera kuthetsedwa. Njira ziyenera kupezeka zothandizira kukuzza chiwerengero cha amayi ochita ndale ku makhonsolo ndi ku boma komwe. Ngati boma lingathe kutumikira anthu ake mokwanira liyenera kumangidwa kuchokera pa luntha la amuna ndi akazi omwe. Liyenera kuvomereza gawo lomwe amayi amakhala nalo pakati pa anthu ndi kufunika koti pazikhala kufanana pakati pa abambo ndi amayi pa ntchito zonse za maudindo akuluakulu.

Pa chifukwa chimenechi, bungwe la Pan African Civic Educators Network (**PACENET**) likufuna kupereka bukhu limeneli kwa amayi omwe akufuna kukhala makhansala kapena aphungu kuti aligwiritse ntchito ngati chipangizo choti chiwathandize kudziwa zinthu zofunika zomwe zingawapangitse kukhala anthu aphindu. Bukhu limeneli lomwe mutu wake ndi *“Kukwaniritsa Kupambana kwa Amayi pa Chisankho”* lapangidwa kuchokera ku bukhu lophunzitsira amayi ofuna kukhala pa mipando ya utsogoleri ngati mbali imodzi yothandiza boma kukwaniritsa chilinganizo chokuza chiwerengero cha amayi m'maudindo akuluakulu ndi ndale. **PACENET** ngati bungwe limadzipereka kwambiri polimbikitsa ganizo loti amayi ambiri azikhala m'maudindo akuluakulu a ndale muno m'Malawi. Cholinga chenicheni cha bukhu ndi kuthandiza inu amayi ofuna kupikisana nawo pa maudindo kuti mukhale omvetsa ntchito ya khansala ndi phungu komanso kukupatsani malangizo okuthandizani kukhala mtsogoleri wa phindu. Bukhu likuperekanso mangizo a momwe mungalowere m'maudindo a utsogoleri posankhidwa ndi momwe mungakonzekere pa ntchito yanu yokopa anthu.

ZOLINGA

1. Kuzindikiritsa mzimayi wofuna kupikisana nawo pa udindo m'mene iyendera khosolo ndi boma m'Malawi.
2. Kuthandiza mzimayi wofuna kupikisana nawo pa udindo kuti athe kuzindikira mwayi womwe ali nawo ndi njira zogonjetsa mavuto okhudza chuma, zoletsa zokhudza chikhalidwe ndi ndale za amayi.
3. Kusonyeza zinthu zomwe amayi ofuna kukhala pa udindo ayenera kudziwa zokhudza udindo ndi ntchito za khansala kapena phungu.
4. Kulangiza amayi ofuna kukhala pa udindo momwe angakonzekere ndi kuchitira ntchito ya phindu yokopa anthu pa chisankho.

GAWO LACHIWIRI: MAWU OTSOGOLERA

Chisankho chitha kutanthauzidwa ngati njira yomwe anthu kapena mabungwe amagwiritsa ntchito pofuna kupeza anthu owatsogolera. Ku mbali ya ndale, chisankho ndi njira yosankhira anthu oyimira anzawo ku boma ndi kuona kuti anthu okhala m'maudindo ndi ovomerezeka kwa anthu ambiri. M'maboma a demokalase monga Malawi zisankho zimapereka mwayi kwa anthu kuti asonyeze kukonda kwawo nthawi ndi nthawi.

Kuno ku Malawi pali mitundu itatu ya zisankho yomwe ndi yovomerezeka ndi malamulo a dziko lino. Zisankhozi ndi za **upulezidenti**, **uphungu** wa ku nyumba ya malamulo ndi **ukhansala**.

Chisankho cha Pulezidenti: Chisankho chomwe anthu amasankha mtsogoleri wa dziko poponya voti mwachinsinsi. Kuno ku Malawi zisankho zonga izi zimachitika kamodzi pa zaka zisanu zirizonse monga m'mene ziliri m'malamulo a dziko lino.

Pulezident: Uyu ndi mtsogoleri wa dziko ndiponso boma yemwe amapatsidwa mphamvu zolamulira dziko. Pulezidenti amasankha nduna zomwe zimamuthandiza potumikira anthu m'ntchito zosiyanasiyana.

Chisankho cha Aphungu: Chisankho chomwe anthu amasankha poponya voti aphungu a ku nyumba ya malamulo owayimira m'madera awo. Zisankho za mtundu uwu zimachitika kamodzi pa zaka zisanu zirizonse molingana ndi malamulo a dziko lino.

Phungu wa ku Nyumba ya Malamulo: Phungu amayimira anthu a dera lake ku boma ndipo amakhala ndi mpando m'nyumba ya malamulo. Udindo waukulu wa nyumba ya malamulo ndiwo kupanga malamulo. Apungu amatenganso madaulo a anthu pa nkhani za chitukuko ndi kupitisa ku boma komanso kufotokozera anthu zomwe boma likuchita kapena kulingalira kuchita. Aphungu amathandiza kuti boma lizichita zinthu zokomera anthu pofunsa mafunso ndi kupempha zinthu zosiyanasiyana.

Chisankho cha maboma aang'ono: Ndi chisankho chomwe amasankha poponya voti atsogoleri a ku makhosolo (**makhansala**) kuti akawayimire ku maboma a kwawo. Zisankho zotere zimachitikanso zaka zisanu zirizonse molingana ndi malamulo a dziko.

Khansala: Khansala amayimira anthu a dera lake pa boma. Makhansala amagwira ntchito zochitukuko m'maboma aang'ono ndi kupanga malamulo oyendetsera makhonsolo (mizinda, matawuni ndi maboma).

Ndi chinthu chofunika kwambiri kuti anthu onse azitenga nawo gawo pa ntchito zoyendetsa boma pofuna kuwonetsa kuti zolinga ndi zofuna za anthu onse zikuganiziridwa. Nkofunika kuchita zofuna za anthu ndi kuchita zinthu mokhulupirika pogwira ntchito za ku makhonsolo ndi za boma. Pa chifukwa chimenechi kayendetsedwe ka boma ndi makhonsolo koganizira kufunika kwa aliyense nkofunika kwambiri. Izi zikutanthauza kuti makhonsolo ndi nyumba ya malamulo zikupereka mwayi kwa aliyense, kuchita zinthu poyera, kuchita zofuna za anthu ndi kuchita zinthu mokhulupirika.

Komabe, vuto lalikulu lomwe lilipo pa kayendetsedwe ka boma labwino koganizira aliyense, kochita zinthu poyera, kochita zofuna za anthu ndi kochita zinthu mokhulupirika ndi kusalabadira kufunika kwa amayi komwe kulipobe. Amayi ndi anthu ofunika kwambiri, amapanga gawo lalikulu la chiwerengero cha anthu a dziko lino komanso gawo lalikulu la anthu oponya voti. Ngakhale zinthu ziri chomwechi, amayi akupitilira kupondezedwa m'maudindo akuluakulu ku makhonsolo ndi ku boma

GAWO LA CHITATU: ZINA NDI ZINA ZOKHUDZA KAYENDETSSEDWE KA BOMA M'MALAWI

Maboma Ang'ono m'Malawi

Maboma aang'ono ndi mbali imodzi ya boma. Maboma aang'ono ndilo tsinde la boma m'Malawi. Mamembala a m'makhonsolo a m'maboma aang'ono amaikidwa ndi cholinga chofuna kukwaniritsa zofuna za anthu ku madera awo, kukonza dongosolo ndi kupeza njira zokwaniritsira zofuna za anthu ndi kudziwitsa boma mavuto omwe anthu ali nawo. Mphamvu zenizeni za maboma aang'ono zagona pa kukhala kwake pafupi ndi anthu ndi kutha kumva ndi kuyankha madandaulo ndi maganizo awo.

Maziko enieni


Mphamvu za boma laling'ono zagona pa kukhala pafupi ndi anthu a kumidzi ndi kutha kumva ndi kutsata maganizo anthu wamba.

Madera a Maboma Aang'ono m'Malawi

Awa ndi madera omwe maofesi a maboma aang'ono otchedwa makhonsolo akhazikitsidwa. Madera amenewa kawirikawiri amakhazikitsidwa potsata lamulo lovomerezedwa ndi nyumba ya malamulo (**Local Government Act**). Komabe ena mwa makhonsolowa anakhazikitsidwa potsata ganizo la pulesidenti. Nduna ya maboma aang'ono imakhalanso ndi mphamvu zolamula kuti dera likhale khonsolo, Kuno ku Malawi tiri ndi madera a maboma aang'ono makumi anayi omwe anagawidwa motere. Makhonsolo a m'mizinda: Blantyre, Lilongwe, Mzuzu ndi Zomba
Makhonsolo a m'matawuni: Balaka, Karonga, Dedza, Luchenza, Salima, Mangochi, Liwonde ndi Kasungu.
Makhonsolo a m'maboma: Balaka, Blantyre, Chikwawa, Chiradzulu, Chitipa, Dedza, Dowa, Karonga, Kasungu, Likoma, Lilongwe, Machinga, Mangochi, Mchinji, Mulanje, Mwanza, Mzimba (Mbwelwa), Neno, Nkhatabay, Nkhotakota, Nsanje, Ntcheu, Ntchisi, Phalombe, Rumphu, Salima, Thyolo, Zomba.

Kodi khonsolo ingachite chiyani?

Mphamvu za makhonsolo zomatha kutumikira anthu ndi kupanga malamulo zimachokera pa lamulo lopangidwa ku nyumba ya malamulo. Lamulo la maboma aang'ono limapatsa mphamvu makhonsolo kuti azitumikira anthu, kupanga malamulo ang'onoang'ono ndi kugwira ntchito zina zirizonse zomwe maboma aang'ono amagwira.



Makhonsolo ali ndi mphamvu zapadera zotsogolera anthu a m'maboma awo moyenera. Izi zitanthauza kuti makhonsolo athanso kuchita zinthu zothandiza kuti anthu a m'maboma amenewa atsogoleredwe moyenera pokhapokha ngati malamulo sawaletsa kutero.

Mphamvu ndi ntchito za khonsolo

1. Kupanga malamulo:

Kupanga malamulo othandiza pa kayendetsedwe kabwino ka dera la khonsoloyo. Kumanga mfundo zoyendetsera ndi kutukula dera la khonsoloyo.

2. Kulamulira:

Makhonsolo amatumikira ndi kupereka zinthu zofunika kwa anthu a m'boma lawo. Amathandiza mabungwe owona za demokalase ndi kulimbikitsa kutenga mbali kwa anthu kupyolera mu kukambirana ndi anthuwo. Kulimbikitsa chitukuko cha zomangamanga ndi cha za chuma kudzera mu dongosolo la chitukuko cha pa boma (**District Development Plans – DDP**). Amalemba, kuphunzitsa, kukweza ndi kudzudzula anthu ogwira ntchito za khonsolo kupatula akuluakulu ndi ma DC omwe amalembedwa ndi kudzuzulidwa ndi a ku likulu la boma.

3. Kutolera ndalama za khonsolo

Pofuna kukwaniritsa ntchito zake, makhonsolo amatolera ndalama kuchokera ku zinthu zosiyanasiyana.

- a. **Misonkho ya malo:-** Iyi ndi misonkho yomwe anthu amakhoma pa chuma chomwe ali nacho ndipo ndi gawo limodzi lomwe makhonsolo amadalira kwambiri potolera ndalama za misonkho yotere.

Makhonsolo amapatsidwa mphamvu kupyolera m'malamulo oyendetsera maboma aang'ono zokhometsa misonkho ya malo. Kuchuluka kwa ndalama zomwe anthu amakhoma pa misonkhoyi kumaganiziridwa ndi makhonsolo omwewo.

- b. **Thandizo lochokera ku Boma:** Makhonsolo amalandira ndalama chaka chirichonse zochokera ku boma ndi cholinga chowonetsetsa kuti makhonsolowo akutha kugwira ntchito zawo.

4. **Ntchito zotumikira anthu:** Ntchito za mtunduwu zimakhudza kupereka kwa anthu zinthu zomwe zikufunika kapena zomwe apempha. Makhonsolo amakhudzidwa ndi madera okhawo omwe ali pansi pawo. Zina Mwa ntchito zomwe amatumikira nazo anthu ndi monga za maphunziro, za Chipatala ndi za umoyo, zosamalira chilengedwe, za miseu, za ulimi, kusamalira ziweto ndi zina ndiponso za malonda.

Boma

Boma linagawidwa mu nthambi zitatu motere:

Pulezidenti ndi nduna - Iyi ndi nthambi yomwe imapangidwa ndi pulezidenti ndi wachiwiri wake kuphatikizapo nduna za boma. Palinso maudindo ena kupatula nduna za boma omwe pulezidenti amasankha kuti akhale gawo la nduna. Anthu onse ogwira ntchito za boma amaikidwa mu nthambi imeneyi.

Nthambiyo imatsogoleredwa ndi pulezidenti yemwe:

Ndi mtsogoleri wa dziko ndi boma;

Ndi mkulu wa gulu la a nkondo la Malawi;

Amasankhidwa zaka zisanu zirizonse pa tsiku lomwe bungwe lochititsa chisankho limasankha.

Atha kukhala pa mpandowu kawiri pa nyengo yotalika zaka zisanu iliyonse.

Atha kusasankhidwanso atalephera chisankho pa mapeto pa zaka zisanu zoyamba kapena pochotsedwa motsata malamulo.

Nyumba ya malamulo- Iyi ndi ntahmbi ya boma yomwe imapanga malamulo yomwe imatchedwa nyumba ya malamulo ndipo imapangidwa ndi aphungu ndi pulezidenti monga mtsogoleri wa dziko. Ntchito yake yaikulu ndiyo kupanga, kukambirana ndi kuvomereza malamulo kuphatikizapo kukambirana ndi kuvomereza kapena kukana dongosolo la chuma choyendetsera dziko.

3. **Nthambi ya za chilungamo-** Awa ndiwo makhothi omwe:- Sakhalira kumbuyo chipani cha ndale, amakhala oyima paokha ndipo amagwira ntchito zawo

m'makhothi omwe amathandiza aliyense powona kuti nthambi zina ziwiri zija zikugwira ntchito zake motsata malamulo.

Amaonetsetsa kuti zinthu zikuyenda mwadongosolo.

Amaweruzana ndi kugamula milandu mopanda kukondera.

Chifukwa chiyani timakhala ndi makhansala kapena aphungu?

Pali zifukwa zambiri zomwe zimachititsa anthu kukhala makhansala kapena aphungu. Ambiri mwa iwo amatchula zifukwa zonga izi:

Amakhala okhutitsidwa akamagwira ntchito zotumikira anthu zomwe amaona ngati ndiyo mphoto yaikulu kwa khansala.

Zabwino zomwe amazipeza ngati membala wa khonsolo monga kukhala wodzindikira m'mene boma liyendera, kukhala wolemekezeka, kukhala wodzidalira poyankhula pa gulu, mwayi womatha kukumana ndi anthu achilendo ndi kukala nawo mu zochitika zomwe sizikanatha kutheka mwa njira ina.

Maganizo ofuna kuyima nawo pa mpando wa khansala kapena phungu ndi kufuna kwa munthu payekha. Komabe munthu wofuna kupikisana nawo pa udindo:

Azikhala woti ali ndi chidwi chothandiza anthu.

Akhale ndi chidwi chofuna kuphunzira luso lomuthandiza kukhala khansala kapena phungu wodalarika monga luso lodziwa kuyankhula bwino pa gulu, kuchita nawo misonkhano, kumvetsa bwino malipoti ndi nkhani za chuma ndi zina zotero.



Ntchito ndi udindo wa khansala

Kutsogolera ndi kulangiza anthu a dera lake;
Kuluzanitsa makhonsolo ndi anthu;
Kupeza uphungu wabwino ndi kupanga malamulo a m'makhonsolo;
Kupereka ku khonsolo nkhanu za chitukuko zokhudza dera lake;
Kulimbikitsa anthu a dera lake kutenga mbali pa zinthu zofunika.

Ntchito ndi udindo wa phungu

Kuluzanitsa boma ndi anthu;
Kupeza uphungu wabwino, kukambirana ndi kupanga malamulo a dziko
Kupereka ku boma nkhanu zokhudza chitukuko cha dera lake.
Kuimira anthu pa zofuna zawo zosiyanasiyana ku nyumba ya malamulo.

Mungakhale bwanji khansala kapena phungu?

Munthu wofuna kusankhidwa kukhala khansala kapena phungu wa ku nyumba ya malamulo:
Ayenera kukhala nzika ya Malawi;
Atha kusakhala nzika ya Malawi koma akhale atakhala m'dziko la Malawi kwa zaka zosachepera zisanu ndi ziwiri.
Akhale atakwanitsa zaka 18 pa tsiku lomwe akulembetsa kuti apikisane nawo;
Akhale munthu yemwe amakhala ku dera lomwe akufuna kuimira, kapena anabadwira komweko, amagwira ntchito ku deralo kapena amachita malonda ku deralo;
Azitha kuyankhula ndi kuwerenga chingerezi bwino kuti akathe kutenga nawo mbali pa zokambirana za khonsolo kapena nyumba ya malamulo popanda chovuta;
Akhale munthu woti kotha silinamugamule kuti alibe chuma;
Akhale atalembetsa m'kaundula kuti adzaponya voti m'deralo;
Asakhale wozungulira mutu;
Asakhale atapezedwa wolakwa ndi kotha pa mulandu wokhudza kusakhulupirika kapena kuchita khalidwe loyipa;
Atha kuthandizidwa ndi chipani kapena kuyima payekha;
Apereke mapepala osonyeza kuti adzaima nawo mu nthawi yake;
Akhale atalipira malipiro ofunika osonyeza kusankhidwa kuti adzaima nawo.

Kokonzekera Chisankho

Malamulo a chisankho

Nkofunika kuti anthu onse ofuna kupikisana nawo pa chisankho azidziwa malamulo achisankho. Malamulowa mutha kuwapeza kuchokera ku bungwe lochititsa zisankho –

Malawi Electoral Commission.

Ufulu ndi Udindo

Munthu wopikisana nawo pa chisankho akhoza kukhalapo powerenga mavoti;
Mutha kusankha munthu woti akakuimireni ku malo oponyera voti;
Mutha kupeza kaundula wa mayina a anthu oponyera voti kuchokera ku bungwe lochititsa chisankho popanda choletsa;
Mutha kukopa anthu kwina kulikonse popanda choletsa malinga mutatsata ndondomeko yake.

Zoti mudziwe

Kodi ndinu wozomerezeke?
Kodi kusankhidwa kwanu nkoyenera?
Kodi mbiri yanu ikukwaniritsa zofunika?
Mudzakhala ndi okuthandizani?

Kodi

mwasankha okuthandizani a zaka zosachepera 18?
mwawalangiza okuthandizani za ufulu ndi udindo wawo?

GAWO LA CHINAYI: GAWO LA AMAYI PA NDALE

N'chifukwa chiyani amayi ayenera kuchita ndale?

Ulamuliro wa demokalase umafuna kuti munthu aliyense akhale ndi mwayi womveredwa kuphatikizapo mitundu yomwe ili ndi anthu ochepa ndiponso amayi. Maguluwa amapanga theka la chiwerengero cha anthu onse choncho thandizo lawo ndi lofunika. Nyira imodzi yolimbikitsa kutenga mbali kwa amayi ndiyo kuwalola kukhala m'maudindo a utsogoleri monga m'zipani.

Izi ndi zina mwa ntchito zomwe amayi angagwire mu ndale:

Kuthandiza pofufuza mavuto omwe anthu akukumana nawo ndi kumanga mfundo. Amayi amagwira ntchito zambiri pakati pathu. Amadziwa mavuto omwe anthu akukumana nawo ndi mayankho omwe akufuna;

Kuthandiza pofalitsa mauthenga – Amayi amatha kusonkhanitsa timagulu ting'onoting'ono ta anthu nkupanga magulu aakulu omwe mavuto awo ndi ofanana nkumatha kuthandiza magulu otero;

Atha kupeza anthu oti ayime nawo pa chisankho – Amayi amakhala otakataka m'makomo awo, m'misika, ku ntchito kwawo ndi ku midzi yawo. Powalowetsa m'maudindo a chipani, amayi atha kufikira anthu ambiri mothandiza chipanicho;

Atha kuyambitsa ntchito zina zomwe zingathandize chipani – Amayi atha kuyambitsa magulu ena okhudzidwa mwapadera mogwirizana ndi magulu ena a amayi (ophunzira, osiyidwa, amalonda, aphunzitsi, alimi, a zaumoyo) kuti athandize chipanicho kukwaniritsa zolinga zake;

Kupanga mikuwo yokopera anthu, zizindikiro za chipani ndi kulengezetsa chipani;

Kuyankhula m'misonkhano;

Kukonza misonkhano;

Kupeza anthu odzipereka ndi otsatira chipani atsopano;

Kufufuza pa zomwe otsutsa akuchita.

Chofunika kwambiri

Amayi azitenga mbali m’maudindo ndi ndale chifukwa mfundo za ufulu wa anthu masiku ano zikuletsa abambo kuphangira maudindo . Zitsanzo za zilinganizo zomwe ziripo zothandiza kutukula kutenga mbali kwa amayi m’maudindo ndi ndale ndi izi:

MFUNDO ZOMWE DZIKO LINO LIKUTSATA

Malamulo oyendetsera boma la Malawi:

Gawo 13 la malamulowa limati:

Boma lidzatukula umoyo wa anthu a mtundu wa Malawi popitiliza kugwiritsa ntchito mfundo ndi malamulo omwe cholinga chake ndi kukwaniritsa zolinga izi:

Kufanana pa jenda

Kuti pakhale kufanana pakati pa abambo ndi amayi kupyolera mu:

Kulola kuti amayi azitenga mbali pa chilichonse chochitika pakati pa anthu ndi cholinga choti azifanana ndi abambo.

Kukwaniritsa mfundo zoletsa kusalana ndi mfundo zina zomwe zingafunikire.

Gawo lina lomwe limaletsa mchitidwe wa tsankho ndilo gawo **20** la malamulo a dziko lino, makamakanso gawo **24** limakamba za ufulu wa amayi motere:

Amayi ali ndi ufulu wotetezedwa ndi malamulo mokwanira ndi mofanana, ndiponso ali ndi ufulu wosachitiridwa tsankho poganizira kuti ndi amayi kapena pokhala okwatiwa kapena osakwatiwa.

Lamulo lirlonse losala amayi pa zifukwa zoti ndi amayi, okwatiwa kapena osakwatiwa silidzagwiritsidwa ntchito ndipo lamulo lidzakhazikitsidwa pothetsa miyambo ndi zochitika zonse zowasankha pa ntchito, pa malonda ndi zochitika za boma.

Mfundo ya Boma pa nkhani za jenda

Lamulo limeneli linakhazikitsidwa m’chaka cha **2000** ndi boma la Malawi ndipo cholinga chake ndi kuphatikiza nkhani za jenda ndi ntchito zotukula dziko lino. Kuwonjezera apo, ndondomeko ya dziko lino pa nkhani za jenda inakhazikitsidwa m’chaka cha **2004** kuti ithandize kukwaniritsa mfundo ya boma pa nkhani za jenda ndi kuwonetsetsa kuti mfundoyi ikugwirizana ndi zolinga za boma pa chitukuko zomwe ziri mu dongosolo la dziko la Malawi lochepetsa umphawi ndi dongosolo la dziko la Malawi pa chitukuko. Chimodzi mwa zolinga za ndondomeko ya dziko la Malawi pa nkhani za jenda ndicho kulimbikitsa ndi kuteteza kutenga mbali kwa amayi pa ndale ndi maudindo ndi ufulu wa amayi.

MFUNDO ZOMWE DZIKO LAPANSI LIKUTSATA

Mgwirizano Wothetsa Tsankho la Mtundu Uliwonse Lochitira Amayi (**The Convention on the Elimination of all forms of Discrimination Against Women- CEDAW – 1987**).

Uwu ndi mgwirizano wa ufulu wa anthu wa bungwe la **United Nations** womwe umaletsa mchitidwe uliwonse wochitira tsankho amayi a dziko lirlonse monga kuwaletsa kuponya voti yofuna kumva maganizo a anthu ndi kuwaletsa kutenga mbali popanga ndi kukwaniritsa mfundo za boma kuphatikizapo kukhala nawo m’zochitika za m’mayiko osiyanasiyana. Mgwirizano wa **CEDAW** umawonetsetsa kuti amayi ali ndi maufulu awa: Kufanana ndi abambo pa ufulu wotha kuponya voti m’zisankho za mitundu yonse; Kutenga gawo pa ntchito yopanga mfundo zoyendetsera boma ndi kukwaniritsa mfundozo; Kukhala m’maudindo a boma ndi kugwira ntchito za boma za mtundu uliwonse; Kutenga mbali m’mabungwe omwe si a boma ndi ena okhudzidwa ndi ntchito zosamalira anthu ndi za ndale mdziko lirlonse.

Mgwirizano Woonu Ufulu wa Amayi pa Ndale (The Convention on the Political Rights of Women – 1952).

Mgwirizanowu umafotokoza kuti amayi ali ndi ufulu woonya voti molingana ndi abambo m’zisankho zomse mopanda kusolidwa kwa mtundu uliwonse. Athanso kusankhidwa pa maudindo aliwonse m’mabungwe osiyanasiyana ndi kutinso atha kukhala pa udindo uliwonse wa boma popanda kuletsedwa.

Mgwirizano wa ku **Beijing** Wolimbikitsa Kuchitapo Kanthu (The Beijing Declaration and Platform for Action).

Uwu unali msonkhano wina wofunika kwambiri womwe unalimbikitsa kufanana pakati pa abambo ndi amayi m’mayiko onse. Dziko lirlonse linadzipereka kukwaniritsa mfundo ina iliyonse yapadera yothandiza kulimbikitsa nkhani za jenda pa dziko lonse lapansi.

d. Mgwirizano wa Mayiko a mu SADC pa Nkhani za Jenda ndi Chitukuko ndi Zina (**SADC Declaration on Gender and Development and its Addendum – 1997**)

Mgwirizano wa SADC pa nkhani za jenda umapempha mayiko a m’derali kukwaniritsa chiwerengero cha **30%** ya amayi m’mabungwe onse opanga malamulo. Mabungwewa ndi monga nyumba ya malamulo, maunduna, makhonsolo, ndi mabungwe ena ogwira ntchito za boma.

GAWO LA CHISANU: MWAYI WOMWE AMAYI ALI NAWO PA NDALE NDI KULIMBANA NDI MAVUTO OKHUZA JENDA

Kodi pali mwayi wanjwa wosankhidwa pa ndale?

Mwayi wa ndale: Mwayi wa ndale utanthauza kupezeka kwa mpata womwe ungalole mzimayi kukwaniritsa zolinga zake zofuna kukhala pa udindo wa ndale kudzera m’chisankho. Mwayi wa mtunduwo womwe wakhala ukupezeka chiyambireni ndale za zipani zambiri m’Malawi m’chaka cha 1990 ndi monga:

Ufulu wokwanira wolola amayi kutenga mbali pa kayendetsedwe ka dziko;
 Ndale za ulamuliro wa zipani zambiri m'malo mwa ndale za chipani chimodzi;
 Kukhazikitsidwa kwa unduna wa chitukuko cha amayi ndi ana womwe umakwanitsa
 ndondomeko za boma zomwe cholinga chake ndi kuthandiza amayi kuti azitenga gawo
 m'maudindo akuluakulu ndi ndale;
 Kukhazikitsidwa kwa mabungwe a amayi ndi mabungwe ena owona za ufulu wa anthu
 omwe akulimbikitsa ufulu wa amayi;
 Kukhazikitsidwa kwa mfundo ya boma pa nkhani za jenda ndi ndondomeko ya boma pa
 ntchito za jenda;
 Kusaina mgwirizano wa mayiko a mu SADC pa nkhani za jenda ndi chitukuko ndi zina
 zoletsa nkhanza zochitira amayi ndi ana;
 Amayi akhala akutsogolera m'mipingo, m'makalabu mu ntchito zopezera ndalama, ntchito
 zodzithandiza ndi mabungwe ena a kumidzi;
 Kupezeka kwa mabungwe othandiza ndi ndalama zothandizira kukweza ndi kutukula
 amayi pa ndale komwe kulipo masiku ano;
 Kuchepa kwa chiwerengero cha aphungu achizimayi;
 Mapangano a m'ziko momwe muno ndi ena a m'mayiko onse omwe boma la Malawi
 lidasaina.

Mavuto omwe alip ndi otani?

Amayi ambiri sanafikebe powona phindu lake posankhidwa kukhala aphungu ngakhale
 pali mwayi womwe wafotokozedwa pamwambapa kamba koti pali zipsinjo zina.
 Ngakhale poponya voti ndi kuyima nawo pa chisankho, amayi amakumana ndi mavuto
 ambiri chifukwa palibe chilungamo chenicheni. Ena mwa mavutowo ndi awa:
 Kusowa kwa zipangizo, anthu owatsatira ndi chuma;
 Kusowa kwa luso lochita ndale monga njira zokopera anthu;
 Kusadziwika pa ndale ndi kusowa mfundo zogwira mtima;
 Zoletsa zina pa ndale monga miyambo ya chikhalidwe. Zokhumudwitsa zotere
 zimapezeka mu zokamba za anthu monga kuwanena amayi ochita ndale kuti ndi anthu
 opanda khalidwe omwe amayerekezedwa ndi anthu olowa ndale ndi cholinga chongopeza
 phindu;
 Kuulutsa nkhani mokondera maka mosakomera amayi ofuna kulowa ndale;
 Amayi ofuna kulowa ndale amakhala anthu otanganidwa ndi mabanja awo poyerekeza ndi
 abambo;
 Amayi amaonedwa ngati anthu omwe amatha kukopa anthu motsogoleredwa ndi abambo.
 Ngati angakwanitse kukopa anthu m'malo mwa abambo, alepheleranji kukopa anthu
 owatsatira pogwiritsa ntchito zipangizo zomwe zilipo?;
 Kulephera kwa boma, mabungwe omwe si a boma ndi magulu ogwira ntchito zomwe si za
 boma pokwaniritsa mfundo ya boma pa nkhani za jenda;
 Mikangano yomwe imakhalapo m'zipani.



MFUNDO ZINA ZOFUNIKA

Kupambana pa chisankho kutanthauza kukhala ndi luso lotha kusankha njira zabwino
 ndi kachitidwe ka ntchito yokopa anthu. Choncho mayi wofuna kulowa ndale ayenera
 kuonetsetsa zinthu izi:
 Njira yabwino yofalitsira mauthenga m'deralo
 Zochitika m'deralo zomwe zimasonkhanitsa anthu ambiri monga maliro, miyambo ya
 chinamwali, maukwati, zikondwelero ndi misonkhano ya m'mipingo. Zitha kukhala njira
 zabwino zofikira pafupi ndi anthu.
 Mabungwe ofalitsa nkhani: pezani manyuzipepala, mawailesi a kumidzi ndi kuwagwiritsa
 ntchito yodziguulitsa nokha kwa anthu.
 Mabungwe omwe si a boma omwe amalimbikitsa ufulu wa amayi m'deralo.

GAWO LA CHISANU NDI CHIMODZI: KUKOPA ANTHU

Kukopa anthu pa chisankho- chochitika chilichonse, mawu kapena zoyankhula zomwe cholinga chake ndi kupezera mavoti munthu aliyense kapena chipani chomwe chikupikisana nawo pa ndale. Cholinga chake ndi kulengeza zolinga za chipani, mfundo zake ndi khalidwe la munthu yemwe akuima pa chisankho m'malo mwa chipani kapena ngati munthu woyima payekha.

Ndani angakope anthu?

Zipani za ndale, anthu ofuna kuima pa chisankho ndi anthu otsatira chipani; Ogwira ntchito za boma, mafumu.

Kumbukirani: Nkosafunika kukopa anthu ngati mulibe wopikisana naye kapena ngati makalata anu osankhidwira sanaloledwe.

Yambani ndi kufufuza anthu odzakuvoterani;

Khalani wozindikira zosowa ndi zithu zofunika kwa anthu;

Khalani wozindikira ndondomeko zoponyera voti.

Kukonzekera ntchito yokopa anthu

Kumbukirani: Kuponya voti pa chisankho ndi kufuna kwa munthu. Musanakope anthu kuti akuvoterani, muyenera kuwalimbikitsa kuti avote.

Pokonza ntchito yokopa anthu, mfundo ziwiri ziyenera kukumbukiridwa:

Anthu adzakuvoterani pokhapokha atakhutitsidwa kuti mungathe kuchita kanthu, sikungogula chabe mavoti ayi;

Mungafune anthu odzipereka kuti akuthandizeni pa ntchito yanu yokopa anthu.

Njira zina zokopera anthu ndi izi:

Kuimbira telefoni anthu ofunika;

Kugawa timakalata;

Kokopa anthu khomo ndi khomo;

Kukumana ndi anthu ku malo komwe kumasonkhana anthu monga ku masitolo, ku malo osangalalira ndi kumisika;

Kulemba nkhani zoti zifalitsidwe m'manyuzipepala;

Kulengezetsa m'manyuzipepala;

Kumveka m'mawailesi;

Kupereka mbiri yanu ku manyuzipepala, mawailesi owulutsa mawu ndi a kanema;

Kuchititsa misonkhano;

Kuyankhula ndi mabungwe ofalitsa nkhani;

Kugwiritsa ntchito zipangizo zaulere zomwe zingakhalepo

Kusankha kwa njira yokopera anthu kumadalira zinthu zingapo. Zina mwa izo ndi izi:

Mphamvu za omwe mukupikisana nawo;

Njira zomwe zilipo zofikira anthu m'bomalo



Nthawi yomwe ilipo chisankho chisanachitike;

Chiwerengero cha anthu okuthandizani omwe mungapeze;

Kukula kwa dera lanu;

Ndalama zomwe muli nazo zokuthandizani pa ntchitoyi

Njira zochitira misonkhano yokopa anthu.

Dziwitsani a DC polemba kalata ndipo kalata ina mutumize kwa mkulu wa polisi m'deralo.

Malo oletsedwa kukopa anthu

Malo okhala asirikali a nkhondo, malo a apolisi ndi ku ndende.

LUSO LOKOPERA ANTHU

Njira zomwe zimagwira ntchito Njira zomwe sizigwira ntchito Kukopa anthu khomo ndi khomo Kuchita misonkhano yosakonzekera Misonkhano (chitani misonkhano kawirikawiri)

Kuchita misonkhano nthawi yomwe palinso zochitika zinaKufunsa mafumu ndi kupereka mphatsoKugula mavotiKupereka zinthu zosiyanasiyana kwa anthu osowaKulonjeza zobodza/kulonjeza zinthu zambiriKukhala nawo pa zochitika zosiyanasiyana (maukwati, maliro, mapemphero ndi zina)Kupikisana nawo m’dera lomwe si kwanu.Kulimbikitsa amayi kuti atenge mbaliKugwiritsa ntchito mawu otukwana.Kulemba zikalata zokopa anthu.Kusonyeza anthu masatifiketi a maphunziro anu,Kulengezetsa misonkhano pa wailesiKugwiritsa ntchito manyuzipeplala ndi wailesi za kanema kumidzi.

ZIPSINJO PA KUKOPA ANTHU NDI NJIRA ZOZITHETSERA

CHIPSINJONJIRA YOTHETSERAMiyambo yachikhalidweOnetsetsani kuti mukumvetsa miyambo ya anthu a dera lomwe mukukopa anthu ndikuyetsetsa kuti musakhulane ndi chikhalidwechoKuopsezedwa ndi abamboYankhulani ndi abambo ndi amayi pa zabwino zomwe mudzachite mukadzakhala pampandoPezani wokutsatirani kapena wokuthandizani kuti akuthandizeni kukopa anthu m’deraloNsanje za amayi kwa mayi mzakePhungu wachizimayi ndi mayi, mlongo zakhali ndinso mkazi wa munthu ndipo amamvetsa mavuto a amayi ena kuposa bamboPezani m’bale wachizimayi kuti akuthandizeniKusowa kwa zipangizo monga mayendedwe, ndalama.Gwiritsani ntchito njira yotsika mtengo ya mayendedwe.Gwiritsani ntchito abale anu pokopa anthu.Funsani amayi ena kuti akuthandizeniPezani njira yopezera ndalama mwanokha.Funsani mabungwe omwe amathandiza amayi.Mafumu omwe amaletsa otsutsa kukopa anthu m’madera awoOnanani ndi a ku banja la mfumuyo a chizimayi.Limbani mtima ndi kupilira, osataya mtima.Gwiritsani ntchito okutsatirani achimunaOpikisana nawoMusawachitire nkhanzaAyamikireni mwachinyengoMchitidwe wosafuna kuvotaPhunzitsani anthu ovota.Auzeni zomwe boma limachita ndi zomwe lingawachitire.

Kuti mukhale wa chikoka.

Khalani wosakaika;
Dzisonyezeni kwa anthu mwaulemu ndi kufotokoza cholinga cha kubwera kwanu. Ngati munthuyo ali wotanganidwa, pemphani nthawi ina;
Khalani wokoma mtima ndi kumvetsera zomwe anthu akufuna kukamba nanu;
Lembani mwatsatanetsatane zofuna za anthu
Chepetsani nthawi yomwe mungataye pa malo kapena ntchito iliyonse;
Konzekerani madandaulo ndipo fotokozani njira yomwe anthu angatsate pa madandaulowo
Fotokozani za yemwe angathe kuvota;

Tsirizani zokambirana zanu popempha chithandizo;
Siyani chikalata chanu – ichi chidzakhala ngati chikumbutso cha kucheza kwanu ndipo siyani zikalata zanu kapena zikalata zofotokoza za chisankho m’makomo momwe simunapezemo anthu.

Kumbukirani

Lemekezani chikhulupiliro chomwe anthu ali nacho pa inu pokufotokozerani mavuto awo ndi maganizo awo. Kukambirana ndi anthu ena a m’mudzimo za mavuto omwe ena afotokoza kale ingakhale njira yabwino yodziwira maganizo a anthu pa zinthu zofunika. Izi zingachitike popanda kutchula mayina a anthu ena omwe akambapo kale.

Zombalemba zokamba za chisankho

Izi zimagawidwa ndi anthu ofuna kuima pa chisankho kapena owaimira kuti adziwitse anthu za cholinga chawo chofuna kuima pa chisankho cha ukhansala kapena phungu. Zolembalembazi zitha kukhala zomata pa khoma timabukhu kapena makalata. Nkofunika kuti zolembedwa zonse zokopa anthu zizikhala ndi chizindikiro cha munthu yemwe akufuna kusankhidwa kapena chipani

Kumbukirani:

Ndi chanzeru kuti mulembe zinthu zanu mu chiyankhulo chomwe anthu ambiri angathe kuchimva.

GAWO LA CHISANU NDI CHIWIRO: KUTHETSA MIKANGANO

Si chinthu chachilendo kuti anthu osiyana akhale ndi maganizo osiyana pa zinthu zosiyanasiyana monga chikhalidwe, zikhulupiliro ndi zochita. Koma tsopano nthawi zina kusiyana maganizo kotere kumafika poyipa kotero kuti mikangano imabuka yomwe imaopseza mtendere pakati pa anthu, magulu a anthu kapena dziko. Mikangano yomwe imadza kamba ka chisankho itha kukhala ndi zotsatira zoyipa pa miyoyo ya anthu, chuma ndiponso ndale ngati italekeleredwa. Gawo lino likufotokoza mitundu yosiyana ya mikangano yokhudza chisankho ndi njira zoithetsera ndi cholinga choti amayi omwe akufuna kukhala atsogoleri akhale odziwa ndi okonzeka ndi luso lothana ndi mikangano yotero.



Mikangano ya chisankho

Mikangano yodza kamba ka chisankho ndi mikangano yomwe imachitika pa nthawi ya chisankho. Mikanganoyi itha kukhala pakati pa zipani kapena anthu opikisana m'dera limodzi la khansala kapena phungu. Mikangano yokhudza chisankho ndi chinthu chimodzi chomwe chimaopseza ufulu wa demokalase ndi mtendere pa ndale m'dziko lililonse. Makhothi owona za chisankho akhala akuweruza pa mikangano yotere kuyambira kale. Koma tsopano makhothi atha kukhala otayitsa nthawi ndi a mtengo wapatali kwa anthu omwe alibe chuma chokwanira. Choncho njira zina zapafupi zothetsera mikangano ziyenera kupezeka. Izi ndi monga kukambirana, kukhala ndi mkhalapakati ndi kuyanjanitsa. Amayi ofuna kukhala atsogoleri ngofunika kumvetsa njira zimenezi podziwa kuti atha kupezeka m'mavuto otere koma alibe ndalama zoti ziwathandize pogwiritsa ntchito makhothi.

Njira zothetsera mikangano ya chisankho

Njira zodziwika bwino zothetsera mikangano ya zisankho m'madera a aphungu kapena makhansala ndi izi:

Kukambirana mwaubale.

Iyi ndi njira yomwe mbali ziwiri zokangana zimakambirana mavuto awo mwaubale. Njirayi itha kuthetsa mkangano womwe ungakhalepo kapena kuchititsa kuti mbali ziwirizo zigwirizane kupeza njira zina zomwe zingathandize kuthetsa mkangano.

Kukambirana mwadongosolo

M'njira imeneyi mbali ziwiri kapena zingapo zimakomana ndi kukambirana mavuto awo motsatira ndondomeko ina yake. Mbali zonsezo zimagwirizana kuti zithetse mkangano wawo pokambirana pamaso ndi pamaso ndi kugwirira ntchito limodzi pofuna kupeza yankho lomwe aliyense mwa iwo agwirizane nalo.

Kukhala ndi mkhalapakati

Njira imeneyi ndi yosiyana ndi njira yokambirana mwadongosolo ndi yokambirana mwaubale chifukwa imakhala ndi wina wachitatu yemwe mavutowo sakumukhudza kukhala ngati mkhalapakati. Mkhalapakati yemwe amakhala wovomerezeka ndi magulu awiriwo, amathandiza kuti maguluwo athe kukambirana mavuto awo ndi kuthandiza kuti agwirizane njira zomwe angamatsate pothetsa mavuto awo.

Komiti yodzetsa mgwirizano pakati pa zipani.

Kukhazikitsa kwa makomiti odzetsa mgwirizano pakati pa zipani m'maboma kwachepetsa kukaikirana pakati pa anthu oyima nawo pa chisankho komanso pakati pa zipani komwe kukanatha kuyambitsa ziwawa zoopsa.

Kusuma ku khothi

Mikangano yodza kamba ka zisankho ndi gwero lalikulu la kusamvana pakati pa anthu ochita chisankho kumidzi ngakhale m'dziko lonse. Ngati mikangano yodza chifukwa cha zisankho siithetsedwa isanafike poyambitsa ziwawa itha kusokoneza chikonzero chonse cha chisankho. Zotsatira za mikangano yotere ndi zambiri. Zina mwa izo ndi kuonongeka kwa katundu, miyoyo ya anthu ndi kuchotsedwa kwa anthu ofuna kuyima nawo pa chisankho. Nthawi zina mikangano ya zisankho ikhoza kutalikitsa chikonzero chonse cha chisankho kapena kubweretsa nkondo za pa chiweniweni zomwe zotsatira zake zitha kukhala zoyipa kwambiri. Kotero ndi kofunika kuti anthu onse opikisana adziletse kuchita zinthu zomwe zingabweretse ziwawa. Ndi ntchito ndi udindo wa onse okhudzidwa ndi chisankho kuteteza kuti mikangano ya chisankho isachitike.

Ena mwa mabungwe omwe akuthandiza kuti padzakhale amayi ambiri pa chisankho cha 2009

Bungwe la Action Aid International ku Malawi

Bungwe la Association for Progressive Women (APW) – ku Mwanza

Catholic Commission for Justice and Peace – m’maboma onse

Centre for Human Rights and Rehabilitation (CHRR) ku Lilongwe

CIDA – GESP

Bungwe la Civil Liberties Committee (CILIC) ku Blantyre

Bungwe la Church and Society Projects of lthe CCAP Synods m’maboma onse

GTZ – MGPDD

Gender Support Programme (GSP) ku Blantyre

Malawi Electoral Support Network (MESN)

Malawi Human Rights Commission (MHRC)

NGO – Gender Coordination Network (NGONCN)

National Women’s Lobby Group (NWLG) ku Blantyre

National Initiative for Civic Education (NICE) m’maboma onse

National Election Support Network (NEST) ku Blantyre

OXFAM

Pan African Civic Educators Network (PACENET) ku Blantyre

Royal Norwegian Embassy (NORAD)

Society for the Advancement of Women (SAW) ku Blantyre

UNFPA

Women’s Voice ku Blantyre

